



April 2016

Okondedwa Abale,

M'mwezi wa Febuluwale, Mulungu anandiitana kuti tigawane za chiyembekezo chodabwitsa cha Yesu Khristu ndi amayi kupyolera mu Project ya Hannah. Ngati mkulu wa tsopano wa utumiki umenewo, ndine okondwera kulandira ntchito yosamalira ndi kutsogolera Project ya Hannah m'masiku akudzawa. Ndikuthokoza kwa Marli Spieker, ndi zikwizikwi za ogwira ntchito komanso anthu ogwira ntchito modzipereka padziko lonse la pansi, Ndikukondwera chifukwa cha maziko olimba amene timangepo.

Ndiyambe ndikuti "zikomo" chifukwa cha mapemphero m'mzaka zonsezi ku Project ya Hannah, ndi kugwiritsa ntchito kalendala ya pemphero potsogolela mapemphero anu. Ndinu mbali imodzi ya anthu apemphero am'maiko 125. Pamodzi tigwiritsa ntchito mapemphero kupyolera muziyankhulo 69 zamuutumiki wapawailesi ndi zitsitimumutso za m'mdera, ndipo tikutha kudziwitsana zofuna za amayi padziko lapansi. Mulungu akugwira ntchito yaukulu ndipo ndili okonzeka kudzaona zomwe watikonzera mtsogolo.

Mwezi uno tikutukulira alongo athu aku Caribbean. Tiyeni tipemphere kuti mitima ikhudzidwe ndipo miyoyo yawo ichilitsidwe mwa Yesu. Akumane ndi chikondi chake m'mitima yawo, monga momwe amachitira akamaona ndi kukondwerera chilengedwe chake chokongola.

Mapemphero anu akutipangitsa kukhalabe olumikizika ku mpesa weniweni amene amatistogolera panjira imeneyi. Popanda mapemphero anu sitikanatha kukwanillitsa ntchito yomwe anatipatsa. Pamene tikupitiliza kupemphera, mitima yathu ndiyokondwere kuti amamva mapemphero athu. Iye amasankha mitima yosweka. Amakhululuka tikalapa. Amapeleka chiyembekezo ndi machilitso kwa onse mwa Mwana wake Yesu (Masalimo 32:21, Masalimo 34:17; 1Yohane 1:9; Yohane 3:16 ndi 15:5).

Ndidzakhalabe othokoza pakudzipereka kwanu kupempherera amayi padziko lonse la pansi. Ndikudziwa kuti Mulungu amawaona ndi kumva kulira kwa amayiwa. Tipitililebe kukhala obweretsa chiyembekezo kwa amayi apadziko lapansi mwa Yesu.

Mwa iye mitima yathu ikondwera,

Peggy Banks  
Nkulu Woyendetsa Utumiki Padziko Lonse  
Project ya Hannah